

## MARKING SCHEME FOR CHICHEWA PEPALA 2

### 1. (a) Mitundu ya agwirizanitsi

- (i) Mgwirizanitsi wamchitidwa ntchito **(Malikisi 1)**
- (ii) Mgwirizanitsi waumwini **(Malikisi 1)**
- (iii) Mgwirizanitsi wamgwirizano/ ubale **(Malikisi 1)**
- (iv) Mgwirizanitsi wamchitantchito **(Malikisi 1)**
- (v) Mgwirizanitsi wamawerengo /mowerengera **(Malikisi 1)**

### (b) Ntchito za mifuwu (yanchito lililonse) **(Malikisi 1)**

- (i) Kudabwa
- (ii) Kudandaula
- (iii) Kukondwa
- (iv) Kukopa chidwi
- (v) Kulimbikitsa

### 2. Nchito za “ndi”

(a) (i) Mwanayu ndi wamwano/ kumeneku ndi kulakwitsa  
Aphunzitsi **(Malikisi 2)**

(ii) Amayi ndi abambo apita kumunda/

- Ophunzira amayimba ndi kuvina usiku onse

(iii) Mpandowu mwamanga molimba kuti ndi! /  
umange nsaluyo kuti ndi! kuti mwana asagwe

(b) Sinthani aneni mziganzo kuti akhale mu msintho wotsutsa

(i) Tsekula chitsekucho

(ii) Iwe yalula pamthunzipo mkekawo

(iii) Ife timatula ngakhale atinene



(iv) Sing'anga watsirikula munda

3. (a) Magulu a mivekero ( Yankho lililonse) (**Malakisi 1**)

- (i) Mvekero wa phatikizo limodzi
- (ii) Mvekero wa maphatikizo awiri
- (iii) Mvekero wa maphatikizo atatu
- (iv) Mvekero wobwerezabwereza
- (v) Mvekero wa maphatikizo anayi

b. Chachikazi ( Yankho lililonse **Malikisi 1**)

- (i) Apongozi
- (ii) Mdzakazi
- (iii) Fumukazi
- (iv) Thadzi
- (v) Ntchembere

4. (a) Mitundu ndi ntchito ya akapandamneni

(i) Mtundu: wadzina (**Malikisi 1**)

Ntchito: kukhala pamtherankhani/kukhala mchitidwanchito

**(Malikisi 1)**

(ii) Mtundu: Wamperekezi (**Malikisi 1**)

Nchito: Kusonyeza (**Malikisi 1**)

(b) Kusintha ziganizo kuti zikhale mu zoyankhula mwini

(Yankho lililonse) (**Malikisi 2**)

(i) “Kodi mukusema chiyani? Iye adafunsa

Mayankho akupitirira/...



- (ii) “Musamaononge zachilengedwe,” Mtsogoleri wathu  
Adatilangiza.
- (iii) “Uzizamala ndi anthu abodza” Amayi adandiuza

### KUMVETSA NKHANI

5. (a) i. Adali ndi cholinga choti amupemphe Ziligone kuti akamuyitanire mkazi wake amene adachoka pakhomo pake. **(Malikisi 2)**
- ii. Kwa a Malambo **(malikisi 1)**
- iii. Ankazunzika ndi umphawi umene gwero lake lidali kusatsatira uchembere wabwino **(Malikisi 2)**
- iv. Ziligone ankadziwa vuto lomwe mkazi wa Salapa adachokera pamene Salapa mwiniwakeyo sankaziwa **(Malikisi 2)**
- v. Anali ndi ana oti atha kuwasamala  
Pakhomo pake panali posasowa kanthu  
Mkazi wake ankaoneka okongola chifukwa choti amasamalidwa bwino. Mayankho awiri okha **(Malikisi 2)**
- vi. Adamuthamangitsa **(Malikisi 2)**
- vii. Pakhomo pake pakakhala njala chaka chilichonse  
Ankalephera kugula zovala za ana ndi mkazi wake **(Malikisi 2)**  
Mayankho awiri okhoza
- viii. Zomwe zidawachitikira a Salapa zobereka ana ambiri sizingasintheke ndiye sibwino kumangozidandaulabe **(Malikisi 2)**
5. (b) (i) **Matanthauzo azinin’ga**
1. Adalawira
  2. Adakanitsitsa
  3. Wandizindikiritsa

Mayankho akupitirira/...



(ii) **Mau ofanana m'matanthauzo**

1. Nkhongono
2. Kusinkhasinka

(6) **Chifupikitso**

**(Mau asachepere 45 koma asapitirire 54)**

Kulumala nkosiyanasiyana / Ena amabadwa olumala pomwe ena atakula kale

Munthu atatha kulumala pangosi zosiyanasina,/ olumala amavutika./ olumala miyendo amavutika poyenda

Palibe amasakha kulumala./ olumala Olumala amadalira osalumala m'zambiri,/ Monga kusamba ndi kudya./ Monga kusamba ndi kudya

Ndi bwino kuthandiza olumala/ molingana ndi vuti lawo. /M'dziko lathu olumala ena amazidalira.

**7. Masulirani nkhani yotsatirayi m'chichewa comvemveka bwino. (Malakisi 15) chagawwidwa m'zigawo, gawo lililonse malikisi 1)**

**CHILD ABUSE AND ITS EFFECTS**

Child abuse is any form of maltreatment by an adult, which is violent or threatening for a child./ It can also mean neglect. / which is lack of love, care and attention to a child./ child abuse can be over a long period of time/ or just one-off action./ It can happen in person or online./

Child abuse may cause/ physical and mental problems./ These problems can lead to anxiety/, depression and substance use disorder. Children may isolate themselves / and have hard time making friends,/ in order to hide the abuse from others.

Mayankho akupitirira/...



**NKHANZA KWA ANA NDI ZOTSATIRA ZAKE (Malikisi 1)**

Nkhanza kwa ana ndi nkhalidwe uliwonse oipa ochitidwa ndi akulu/ omwe uli ozunza kapena kuopsyeza kwa anawo,/ Zithanso kutanthauza kunyalanyaza,/ komwe ndikusaonetsa chikondi, chisamaliro komanso kulabadira za mwana./ Nkhanza kwa ana zimatha kuchitika kwa nthawi yayitali/ kapena nthawi imodzi./ Zitha kuchitika pamaso kapena pa intaneti.

Nkhanza kwa ana zitha kubweretsa / mavuto akuthupi ndi m'malingaliro./ mavuto amenewa amapangitsa nkhwawa,/ kukhumudwa ndi vuto lakugwiritsa ntchito mankhwala osokoneza bongo./ Ana akhoza kumadzipatula/ komanso kulephera kuti apeza anzawo ,/ ndi cholinga choti abise nkhanza zomwe ena amawachitira.